وضو اور سائنس (Chichewa)



# Wudu Ndi Sayansi

Shaykh-e-Tareeqat, Ameer-e-Ahl-e-Sunnat,
muyambitsi wa Dawat-e-Islami, Allamah Maulana Abu Bilal
**MUHAMMAD ILYAS**
**Attar Qaadiri Razavi**

Translated into chichewa by
**Translation Department**
(Dawat-e-Islami)

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ، وَالصَّلٰوةُ وَالسَّلَامُ عَلٰى خَاتَمِ النَّبِيّٖن،
اَمَّا بَعْدُ، فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ، بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ۔

## Du’a yowerengera bukuli

Werengani Du’a yosatirayi (Pempho) musanayambe kuwerenga buku lililonse la chipembedzo kapena buku la chisilamu, mudzakumbukira chilichonse chomwe muzawerenga, اِنْ شَآءَاللّٰه عَزَّوَجَلَّ:

اَللّٰهُمَّ افْتَحْ عَلَيْنَا حِكْمَتَكَ وَانْشُرْ
عَلَيْنَا رَحْمَتَكَ يَا ذَاالْجَلَالِ وَالْاِكْرَام

### Tanthawuzo

**O Allah عَزَّوَجَلَّ Titsegulireni khomo la nzeru komanso la kuzindikira ndipo mutichitire chifundo, O! inu yemwe ndi wolemekezeka komanso Wawulemerero.**

*(Al-Mustatraf, vol. 1, pp. 40)*

**Dziwani:** Mfunireni zabwino Mtumiki (Salat-'Alan-Nabi ﷺ) kamodzi kumayambiririo komanso kumapeto kwa Du'a.

وُضُو اور سائنس (شافعی)

Wuzu aur Science (Shafi'i)

# Wudhu ndi Sayansi (Shafi


**Kumasulira Nthambi (Dawat-e-Islami)**

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagran, Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

**UAN:**☎+92-21-111-25-26-92 – Ext. 1262

**Email:**🖃kumasulira@dawateislami.net



**Wudhu ndi Sayansi (Shafi'i)**

kumasulira kwa 'Wuzu aur Science mchichewa(Shafai'i)'


◆


MAWUMWINI ONSE NDI OTETEZEDWA

UMWINI © 2025 MAKTABA-TUL-MADINAH

PALIBE GAWO LILILONSE LA BUKHULI LOMWE LINGASINDIKIZIDWENSO, KAPENA KUFALITSIDWA MWANJIRA INA ILIYONSE NGATI, PAKOMPYUTA, PAMAKINA,

KUJAMBULA KAPENA MWANJIRA INA, POPANDA CHILOLEZO CHOLEMBEDWA NDI MAKTABA-TUL-MADINAH.

**Kufalitsa koyamba:** Rabi'-ul-Awwal, 1448 AH – (26,08, 2025)
**Ofalitsa:** Maktaba-tul-Madinah
**Kuchuluka:** -
**ISBN:** -

## Thandizo

Chonde khalani omasuka kulankhulana nafe ngati mukufuna kuthandizira kusindikiza buku lachipembedzo kapena kabuku kuti likhale Isal-e-Sawab ya achibale anu omwe anamwalira.

**Maktaba-tul-Madinah**
Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah MahallahSaudagran,
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

✍ **Email:** maktabaglobal@dawateislami.net – maktaba@dawateislami.net
✆ **Phone:** +92-21-34921389-93 – 34126999
💻 **Web:**www.dawateislami.net

# ZANKATIMU

Wudhu ndi Sayansi (Shafi'i) ........ 1
Ubwino wowelenga Salat ........ 1
Seminare imene inachitika ku Zambwe kwa Germany ........ 1
Wudhu ndi kuthamanga kwa magazi ........ 2
Wudhu ndi nthenda yogwira Ziwalo ........ 3
Yemwe amagwiritsa ntchito miswak ........ 4
Ukafuna [ kukhala ndi ] ubongo wa mphamvu ........ 5
Ma Hadith awiri olimbikisa kugwiritsa ntchito miswak ........ 6
Machilitso ku mathudza a mkamwa ........ 6
Kuyipa kogwiritsa ntchito brashi ya mano ........ 7
Mumaziwa kagwiritsidwe ntchito ka miswak? ........ 8
Ngale 19 za Madani za luntha pogwiritsira ntchito miswak ........ 8
Ubwino osamba m'manja ........ 13
Ubwino wochukucha mkamwa ........ 14
Ubwino wopukuta mkati mwa mphuno ndi madzi ........ 15
Ubwino wosambisa ndi kutsuka nkhope ........ 16
Chitetezo ku Khungu ........ 17
Ubwino wosambisa zigong'ono ........ 18
Ubwino wosambisa ndi kutsuka phazi ........ 19
Madzi osala popanga wudhu ........ 19
Munthu kufika ku Mwezi ........ 20
Choziziswa chogawa mwezi pakati ........ 23



www.dawateislami.net

Chifukwa cha Allah Wamphamvu zonse basi ................................24
Ngale ya Madani ya njila ya Usufi ...................................................25
Sunnah siyikufunikira chitsimikizo cha sayansi.............................26



www.dawateislami.net

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ وَ الصَّلٰوةُ وَالسَّلَامُ عَلٰى سَيِّدِ الْمُرْسَلِيْنَ
اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ ؕ بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ ؕ

# Wudhu ndi Sayansi (Shafi'i)

Werengani mawuwa mpaka kumaliza amene ali ndi matsamba okwana 24. اِنْ شَآءَ اللّٰه ! Muzatenga uthenga wofunikira kwambiri wa Wudhu.

## Ubwino wonfunira zabwino Mtumiki

Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, ' Anthu awiri amene amakondana chifukwa cha Allah Wamphanvu zonse akumana komanso kugwirana chaza ndikunfunira zabwino Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, machismo awo am'mbuyo komanso mtsogolo amakhulukidwa asanasiyane.'

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Seminare imene inachitika ku Zambwe kwa Germany

Mu mayiko omwe ali ku Zambwe, nthenda ya kuvutika m'maganizo ikuchuluka komanso mothamanga kwambiri. Anthu akuvutika kwambiri ndi nthenda ya kusokonekera kwa ubongo ndipo zipatala zowona matenda opasirana zikukhazikisidwa zochuluka kufuna kuthana ndi nthendayi. Mizere yochuluka ndi yayitali ya anthu amene akuvutika

m'malingaliro awo ili ponseponse mu zipatala zikulu zikulu komanso zazing'ono. Dotolo wina waku Pakistani woyang'ana nthenda za m'malingaliro, yemwe ali ndi dipuloma kuchokera ku Zambwe kwa dziko la Germany, anatero mu seminaru pa mutuwu 'Njira zina zomwe zili ndi kuthekera kopewera nthenda ya mumalingaliro kupatula mankhwala' inachitikira ku Zambwe kwa dziko la Germany. Dotoloyu anapanga kafukufuku ndikupeza zimenezi, ndipo anati, "Ndinawalangiza odwala amene amavutika ndi nthenda ya m'maganizo kuti azitsuka nkhope zawo ndi madzi kasanu tsiku lililonse. Anatsatira malangizo anga ndipo patadusa nthawi yochepa, kudwala kwawo kunasintha. Ndinalilangizanso gulu lina la odwala limene linali kudwala nthenda yomweyi kuti azisuka nkhope zawo ndi madzi, komanso manja ndi mapazi kasanu pa tsiku. Anthuwa anasonyeza kusinthika kwakukulu pakuchepa kwa nthendayi." Kumapeto kwa kafukufuku wake, dotoloyu anapeza kuti nthenda ya kuvutika m'malingaliro inali ndi chiwelengero chochepa maka maka kwa Asilamu chifukwa cha kusuka kwawo m'manja, nkhope komanso mapazi [i.e. kupanga Wudhu] kawiri kawiri tsiku lililonse.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب　　صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Wudhu ndi kuthamanga kwa magazi

Katswiri woyang'ana za ntima analankhura motsindika kuti, "Ngati munthu yemwe akudwala nthenda yoopsa wapanga

Wudhu kenako nayezedwa kathamangidwe ka magazi ake, mulingo wakuthamanga kwa magazi ake umayenera kuchepa kuyelekeza ndi poyamba." Malingana ndi Katswiri wa Chisilamu woyang'ana za matenda a m'malingaliro yemwe anati, "Wudhu ndi mankhwala abwino okhawo amene munthu angapange pofuna kuziteteza komanso kuchila ku nthenda ya m'malingaliro." Akatswiri aku Zambwe analangizanso odwala matenda a m'malingaliro kuti azisambisa ziwalo za thupi lawo monga momwe amachitila Wudhu kochuluka pa tsiku lililonse.

## Wudhu ndi nthenda yogwira Ziwalo

Lamuro losambisa ziwalo pa thupi pamene munthu akupanga Wudhu lilinso ndi kufunikila kwakukulu. Kusambisa manja kumayambiliro, kumazindikilisa ndi kukonzekelesa thupi lathu ku mantha omwe amaza kamba ka kuzizila kwa madzi, zimene zimapangisa kuti nkhope komanso ubongo umve kuzizila mu mulingo woyenera komanso pang'ono pang'ono. Lamuro, ngati kusambisa manja koyambilira, kenako kutsuka m'kamwa, kutsuka mu mphuno kenako kusambisa nkhope ndi ziwalo zina za pathupi, zimathandizira kupewa nthenda yogwira ziwalo. Ngati munthu wasambisa mapazi kenako kumalizira kusambisa nkhope ndi mutu wake, pali kuthekera kwa kudwala nthenda zosiyanasiyana komanso Wudhu sungatheke chifukwa cha kusatsatira ndondomeko yake yolondola.

## Yemwe amagwiritsa ntchito miswak

E inu omukonda Rasool! Pali ma Sunnah mu Wudhu ndipo Sunnah iliyonse ndi phata la madalitso. Tingokamba chitsanzo chogwiritsa ntchito Miswak. Aliyense akuziwa kuti ndi Sunnah kugwiritsa ntchito Miswak pamene munthu akupanga Wudhu. Mawu angasonyeze motani m'dalitso wa Sunnah imeneyi! Munthu wopanga Malonda anati,"Ndinakumana ndi munthu yemwe anali Chisilamu posachedwapa. Ndinamupasa miswak ngati mphaso kwa iye. Mwansangala anayilandira nayipukutira pa maso ake pambuyo poyiphyophyona. Mosakhalisa misonzi inayamba kuyendelera m'maso mwake. Iye kenako anatulutsa kansalu ka m'manja ( handkerchief ) kuchokera nthumba lake nakapinda. Pomwe anayamba kukamasula kansalu ( handkerchief ) kake kaja, anapeza kachiduswa ka Miswak pafupifupi ma inches awiri kutalika kwake. Ndipo iye anati, 'Pomwe ndinalowa Chisilamu, Asilamu anandipasa mphatso imeneyi. Ndinali kuyigwiritsa ntchito mosamala kwambiri mpaka inali itasala pang'ono kutha. Ndinayamba kudandawula kwambiri, koma Allah Wamphanvu zonse anali ndi chifundo chachikulu pa ineyo kufikira lero mwandipatsa miswakiyi.' Anapitiriza kufotokoza kuti, 'Ndakhala ndikuvutika ndi kusintha komanso ziseyeye za mano anga kwa nthawi yayitali ndipo dotolo wa dela lathu sanakwanise kundithandiza vutoli. Ndinayamba kugwiritsa ntchito Miswakiyi ndipo ndinayamba kupeza bwino kwakukulu m'masiku ochepa chabe. Pomwe ndinapitanso kukawonana ndi dotolo, anali wodabwa kupeza

kuti ndinachira. Dotolo anati sizinali zotheka kuti ndingochira mu nthawi yechepa chotele ndi mankhwala amene iye anapeleka. Anandiwuza kuti ndikumbukire chomwe ndinali kugwiritsa ntchito. Pamene ndinalingalira mozama, ndinakumbukira ndikuzindikira kuti ndinalowa Chisilamu ndipo umenewu ndi m'dalitso wa Miswak. Pomwe ndinawonesa miswak kwa dotoloyu, anali kuyang'anisitsa ndi chidwi kwambiri mothedwa nzeru ndikuthokoza.'"

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Ukafuna [ kukhala ndi ] ubongo wa mphanvu

Okondedwa abale achisilamu! Kugwiritsa ntchito miswak kuli ndi ubwino wochuluka kwambiri pano pa dziko la pansi komanso pa chipembezo. Imakhala ndi mankhwala komanso zinthu zochuluka nkati mwake zimene zimathandizira kupewera mano kukuwonongeka kwa ntundu wina uliwonse. Zanenedwa mu buku lotchedwa *Haashiyah Tahtaawi,* 'Kugwiritsa ntchito Miswak kumathandizira kaganizidwe komanso kugwira ntchito bwino kwa ubongo, kuchepetsa kupweteka kwa mutu, kumamasula misempha ya m'mutu, kumachotsa phlegm, kumathandizira kupenya bwino, kumathesa mavuto a m'mimba komanso kuthandizira kagayidwe kabwino ka chakudya m'mimba. Kumawonjezera nzeru, kumachulukisa kuthekera kwa kubereka ana kwa

munthu, kumachepetsa kupweteka komanso kumawonjezera kuwongoka kwa msana.

## Ma Hadith awiri olimbikitsa kugwiritsa ntchito miswak

- Pamene Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali kulowa m'nyumba yake yodalitsika, iye صَلَّى اللهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali kugwiritsa ntchito miswak moyambirira.
- Pamene Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali kudzuka pogona, iye صَلَّى اللهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali kugwiritsa ntchito miswak.

[1] Hashiya Tahtawi, Kitab Al-Taharah, p. 69, Dar-ul-Kutub Ilmiyyah Beirut

[1] Muslim, Kitab Al-Taharah, p. 114, Hadith 253, Dar-ul-Kutub Ilmiyyah Beirut

[1] Abu Dawood, Kitab al-Taharah, p. 25, Hadith 57, Dar-ul-Kutub Ilmiyyah Beirut

## Machilitso ku mathudza a nkamwa

Madotolo analankhula kuti, "Nthawi zina chifukwa cha asidi yemwe amapezeka m'mimba komanso kutentha, zilonda zimayamba ndikubadwisa tizilombo (germs) tomwe timafalikira nkamwa monse. Ngati njira imodzi yochiritsira,

tsukani mano anu ndi miswak nkamwa ndipo yendetsani malovu akewo nkamwa kwa kanthawi. Odwala ochuluka adzachira pochita zimenezi."

## Kuyipa kogwiritsa ntchito brashi ya mano

Kutengera kafukufuku, 80% ya matenda amayamba ndi zoyipa zomwe zimapezeka m'mano owonongeka ndipo m'mimba mumawonongeka ndi zoyipazi. Nthawi zambiri ngati sitikusamalira nkamwa mwathu, tizilombo tochuluka timakula nkati mwa changu. Tizilomboti timafalikira nkati mwa mimba yathu ndikuyambitsa nthenda zosiyanasiyana zambiri. Kumbukirani! Burashi ya mano siyingafanane ndi miswak. Akatswiri anapeza komanso anakhazikitsa chimenechi:

- Pambuyo pogwiritsa ntchito brash ya mano kamodzi, tizilombo tochuluka timasalira ku ntengo wa burashi ya mano. Tizilombo timeneti sitimachoka ngakhale kutsuka chinthucho ndi burashi, koma m'malo mwake, zimapitirira kukula mu burashi momwemo.

- Burashi ya mano imawononga kunyedzimira kweni kweni kwa mano.

- Kugwiritsa ntchito burashi ya mano kumawononga chavu pang'ono pang'ono zimene zimayambisa kuti pakhale mipata pakati pa mano ndi chavu. Tiziduswa ta zakudya timasalira m'mipata. Tiziduswa timeneti timaola ndipo tizilombo tija timakula m'mipata muja. Zotsatira zake,

matenda ochuluka a maso komanso a mitundu yina imayamba. Kupenya kwa diso kumabwelera mphanvu kapena munthu amatha kukhala kumene wa khungu.

## Mumadziwa kagwiritsidwe ntchito ka miswak?

Mutha kumaganiza kuti mwakhala mukugwirisa ntchito miswak kwa zaka zochuluka, koma mano anu komanso m'mimba mumakhala mukupweteka munjira zosiyanasiyana. Wokondedwa m'bale mChisilamu! Ndi vuto lako, osati la miswak. Ndinazindikira kuti ndi anthu ochepesetsa kwambiri mwinanso ndi m'modzi mwa anthu zikwi zikwi kumene yemwe amazindikira komanso kugwiritsa ntchito miswak moyenera. Nthawi zambiri timagwiritsa ntchito miswak mopupuluma, mumangopanga Wudhu kenako ndikumapita. Mwanjira ina, sitimatsatira njira zolondola zakagwiritsidwe ntchito kake, m'malo mwake timangopanga ngati chikhalidwe.

## Ngale 19 za Madani za luntha pogwiritsira ntchito miswak

Ma Hadith awiri a Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

- ❖ Kupemphera ma Rak'aat awiri pambuyo poti munthu wagwiritsa ntchito miswak ndi zopambana kuposa yemwe wapemphera ma Rak'aat makumi asanu ndi awiri asanagwiritse ntchito miswak.

- ❖ Onesetsani kuti mukugwiritsa ntchito miswak chifukwa imayeletsa nkwamwa mwanu ndipo zimamukondweretsa Allah Wamphanvu zonse.

(Musnad imam Ahmad Bin Hambal,vol 2,pp.438,Hadees 5869)

*Sayyidunah Ibn 'Abbas (Allah asangalale naye) anati: Miswak ui ndi ubwino khumi. Umayeretsa n'kamwa, umalimbitsa nkhama ndi maso, umachotsa kakala ndi fungo loyipa n'kamwa, umasangalatsa angelo, umawonjezera ntchito zabwino ndipo umakhazikitsa mimba. Koposa zonse, ndi njira yopezera chisangalalo cha Allah ndiponso ndi Sunnah.*

*(Jam'-ul-Jawami'lis-suyuti,vol.5.pp 249 Hadees 14867)*

*Sayyidunah Imam Shaafi'i* رَحْمَةُ اللّٰہِ عَلَیْه *ananena kuti, 'Pali zinthu zinayi zomwe zimakulitsa nzeru za munthu: Kupewa kulankhula zopanda pake, kugwiritsa ntchito Miswak, kuyanjana ndi anthu olungama komanso kutsatira maphunziro achisilamu amene munthu ali nawo.'*

*(Hayat-ul-Haywan lid-Dameeri,vol.2,pp.166)*

*Fanizo:* Sayyiduna Abdul Wahhab Sha'rani رحمة اللّٰهِ عليه anafotokoza kuti: Sayyiduna Abu Bakr Shibli Baghdadi رحمة اللّٰهِ عليه anafufuza miswak pamene amafuna kupanga Wudhu. Iye anayng'ana yang'ana koma sanathe kupeza. Potsiriza, iye رحمة اللّٰهِ عليه anagula miswak ndi dinari imodzi, mwachitsanzo ndalama ya chitsulo ndikugwiritsa ntchito. Anthu ambiri anamutenga ngati ndi wowononga, "Wawononga ndalama zochulika. Ndani yemwe angapereke ndalama zochuluka chotere kugula miswak?" Iye رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anayankha "Dziko lonse komanso zonse zimapezeka nkati mwake sizili kanthu ngakhale pang'ono monga kochepa kwa phiko la udzudzu kuyelekeza ndi kufunikira kwa Allah Wamphanvu zonse. Ngati, pa tsiku la Chiweluzo, Allah Wamphanvu zonse akandifunse – chifukwa chani ndinasiya ma Sunnah a Mtumiki wanga Wokondedwa? Chuma chomwe ndinakupasa sichinali chofunikira kwa ineyo ngakhale pang'ono ngakhale ngati phiko limodzi la udzudzu. Chifukwa chani sindinagwiritse ntchito chuma chochepa ndinali nacho mukupanga ndikukwaniritsa ma Sunnah ofunikira ngati amene aja (kugwiritsa ntchito miswak) – ndiye ndizanena chani?'

- Anthu ophunzira kwambiri Chisilamu anati, "Munthu yemwe amagwiritsa ntchito miswak azawerenga Kalimah pa nthawi yawo yomwalira ndipo yense wotsatero sazakwanitsa kuwerenga Kalimah pa nthawi yomwalira."

- Miswak yabwino ndi Miswak yopangidwa kuchokera ku ntengo wa Peelu, ntengo wa tende, ntengo wa olive, ntengo uliwonse womwe ukutulutsa fungo labwino ndipo kenako mitundu ina yosala ya mitengo.

- Kugwiritsa ntchito ntengo wa miswak pamodzi ndi khungwa lofewetsedwa komanso lowumilapo ndi kwabwino kuyelekeza ndi kugwiritsa ntchito ntengo uliwonse ngakhale utakhala owuma komanso kugwiritsa ntchito miswakiyo pamodzi ndi khungwa la ntengo wina chabe wawuwitsi ndi kwabwino kuyelekeza ndi ntengo ngati womwewu koma wowuma.

- Ndi Makruh kugwiritsa ntchito miswak kuchokera ku ntengo wa bazelo (basil).

- Ndi Makruh kugwiritsa ntchito miswak yayitali kupyola kutalika kwa nkono ngati momwe zinanenedwa kuti ngati miswak ili yayitali kupyola pa mulingo wa nkono, Satana amakhalapo.

- Yendetsani mokwecha miswak pa mano anu a pansi.

- Pamene mwatsimikiza kugwiritsa ntchito Miswak, gwiritsani kosachepela katatu.

- Gwirani miswak yanu ku dzanja la manja kufikira kuti chala chanu chaching'ono chisale pansi, zala zanu zitatu za pakati zikhale pa mwamba pa miswak pomwe chala

chanu chachikulu chisale chilozele molunjika pa mwamba [moyandikira gawo la miswak imene limatsuka mano athu].

- ❖ Poyambirira tsukani mano anu a m'mwamba kumbali ya kumanja kenako ku manzere. Tsukani mano anu a pansi ku mbali ya kumanja kenako ya kumanzere.

- ❖ Kugwiritsa ntchito miswak ndi Sunnah Muakkadah popanga Wudhu, kuyimika Salah, kuwerenga Quran komanso kupeza ndi kuphunzira maphunziro a Sharia. Ndi Sunnah Muakkaadah pamene fungo kapena ntundu wa n'kamwa mwanu mwasintha pambuyo pomaliza kudya zinthu zafungo kapena kudzuka kuchokera ku tulo, pomwe mano anu asanduka ntundu wa chikasu, musanagone, pambuyo poti mwadzuka, pa nthawi yolowa mu Masjid kapena m'nyumba, pomwe muli pa Sahari komanso pamene mwayamba kunva ululu wa kupweteka kwa infa.

- ❖ Tsonga yanu ya miswak ikuyenera kukhala yofewa. Tsonga yolimba izapangisa mano anu kukhala ndi mipata mu Khama lanu.

- ❖ Dulani tsonga zakezo tsiku lililonse chifukwa zimagwira ntchito yake bwino zikakhala ndi chiwisi cha kuwawa kwakeko.

- Ngati miswak yanu yafika poti siyingagwiritsidwenso ntchito, osayitaya chifukwa ndi chida chimene mwagwiritsa ntchito mukupanga Sunnah. ukwirireni pena pake.
- Kugwiritsa ntchito miswak poyigwira mutafumbata zala zanu ngati chibakela kutha kupangisa miswak yanu kupanga ntolo.

## Ubwino osamba m'manja

Popanga Wudhu, manja amasambitsidwa poyambirira. Werengani ndi kuziwa kufunikira kotero: Munthu amagwiritsa ntchito dzanja pogwira zinthu zochuluka. Zotsatira zake, zinthu zosiyanasiyana komanso tizilombo toyambitsa matenda ambiri timakhuzana ndi dzanjalo. Ndipo ngati manja sanasukidwe bwino lomwe tsiku lililonse, matenda a pakhungu ngati ali m'mutsiwa atha kumugwira munthu nthawi yomweyo

1. ziphuphu
2. kusasangalala kwa khungu
3. kuyabwa kwa khungu
4. nthenda yoyamba ndi tizilombo
5. Kusintha kwa ntundu wa khungu, ndi zina zotero. Pamene tasamba m'manja, kuwala kumayamba m'malo onse olumikizirana mafupa ndikuyambitsa kuzungulira

bwino kwa nyesi ya mthupi mwathu. Nyesi imeneyi imasonkhana m'manja mwathu kufikira kuti manjawa amayamba kuwoneka bwino komanso kukongola.

## Ubwino wochukucha nkamwa

Choyambirira, manja amasambitsidwa ndi cholinga choti akhale otetezeka ku tizilombo toyambitsa matenda; kupanda ichi, tizilombo timeneti titha kumalowa m'mimba mwathu pamene tikuchukucha nkamwa ndikufika m'mimba mwathu, kotero kuyambitsa ndi kukolezela matenda ochuluka. M'pweya umene timalowetsa ifeyo nkati mwathu popuma uli ndi tizilombo toyipa toyambitsa matenda kwa ifeyo. Zotsalira za chakudya zimasalira mu n'kamwa mwathu komanso m'mbali mwa mano ndi mate athu. Ndi chifukwa chake tikuyenera kuchukucha nkamwa komanso kupanga Miswak pamene tikupanga Wudhu ndikusamalira nkamwa mwathu bwino lomwe. Ngati nkamwa mwathu simunasukidwe, tingathe kukumana ndi mavuto a nthenda izi:

1. Matenda a Edzi (AIDS) – Chizindikiro chake choyambirira kumakhala kutuluka kwa munthu tizilonda nkamwa. Ma Dotolo akanika kupeza mankhwala ochiza matenda a Edzi. Chifukwa cha matendawa, chitetezo cha mthupi mwa wodwala sichimakwanitsa kuthana ndi nthenda ndipo amamwalira.

2. Kuthetheka kwa mulomo

3. Fungo loyipa la nkamwa komanso milomo

4. Matenda omwe amayamba ndi tizilombo totchedwa Fanga (fungal) komanso matudza, ndi ena ambiri. mu nkamwa. Ngati munthu sakusala kudya, akuyenera kuthira madzi ku m'melo kuwonjezela pa kuchukucha nkamwa mwake. Munthu yemwe amathira madzi ku m'melo kwake kawiri kawiri sadzagwidwa matenda osiyanasiyana kuphatikizapo matudza omwe amatuluka ku m'melo komanso nkhansa ya kholingo.

## Ubwino wopukuta nkati mwa mphuno ndi madzi

Mapapo a munthu amafuna m'pweya omwe ulibe tizilombo toyambisa matenda, usi komanso fumbi pang'ono ndi 80% chinyezi. Kuti thupi lipange ndi kukhala ndi m'pweya wotelewu, Allah Wamphanvu zonse anatidalitsa ife potipatsa mphuno. Pofuna kupangitsa chinyezi m'pweya, mphuno umapanga mulingo wochuluka wa galoni wozaza ndi chinyezi tsiku lililonse. Tsitsi la m'mphuno limatsuka komanso kugwira ntchito zina zikulu zikulu. Mumakodwa tizilombo tosawoneka ndi maso komanso tsitsi ling'ono ling'ono mu mphuno. Tsitsi limeneli limapha tizilombo topezeka mu m'pweya. Kuwonjezera apo, tsitsi limeneli limawonjezeranso chitetezo mu mphuno chimene chimatchedwa kuti Lysozyme chimene mphuno imateteza maso kuti asatenge komanso kukhuzika ndi matenda.

ٱلْحَمْدُ لِلّٰه Yense amapanga Wudhu komanso kupukuta madzi m'mphuno, chiwalo chofunikilachi (mphuno) imatsuka ndikuyela. Zinthu za magetsi zomwe zili za madzi zimathandizira kugwira ntchito kwa tsitsi lanu la pathupi ndipo ndi chifukwa chake Msilamu amakhala wotetezeka ku matenda osiyanasiyana a m'mphuno chifukwa cha kupambana kwa kupanga Wudhu. Kutsuka m'mphuno (m'mene timachitila popanga Wudhu) ndikofunikila kwambiri kwa wodwala yemwe akuvutika ndi chifuwa chosatha komanso mabala mu mphuno.

## Ubwino wosambisa ndi kutsuka nkhope

Masiku ano, kuononga chilengedwe komwe kumaza kamba ka usi smoke ndi zina zotelo. kukuchulukira mu m'pweya. Zinthu zosiyanasiyana za mankhwala, zikusonkhesela ndi zina zotero. zimasonkhana pa nkhope komanso maso munjira ya lisilo komanso fumbi. Kuyisiya nkhope yosatsuka ndi madzi kumapangitsa nkhopeyo komanso maso kugwidwa ndi nthenda zosiyanasiyana. Dotolo waku Europe analemba maganizo ake pa mutu woti 'Diso, madzi ndi thanzi'. M'maganizo ake, anatsindika kuti, "Muzitsuka maso anu tsiku lililonse mowirikiza; apo ayi, mudzakhala mukugwidwa ndi matenda owophya ochuluka.' Kusuka ku nkhope kumateteza kapena kuchepetsa chiwophyezo chotuluka munthu ziphuphu. Akatswiri oyang'ana za tizilombo anagwirizana pakupeza kwawo kuti mitundu yonse ya mafuta ozola amasiya

madontho pa nkhope. Pofuna kupanga nkhope yathu kukhala yowoneka bwino, ikuyenera kumasukidwa nthawi zonse. Katswiri wina, yemwe ndi membela wa 'Khonsolo yowona kukongora ndi chisamaliro cha bwino cha anthu ku America', anapeza kuti, "Asilamu sakufunikira mafuta amankhwala a kumaso chifukwa nkhope zawo zili zotetezeka ku matenda osiyanasiyana kamba kakusambitsa nkhope zawo pamene akupanga Wudhu." Akatswirinso a chitetezo cha chirengedwe anayikiranso ndemanga pa nkhaniyi ponena kuti, ' Munthu akhale wotetezeka ku nthenda zogwira ku maso, munthu akuyenera kusambitsa nkhope yake kawiri kawiri.' اَلحَمدُ لِلّٰه, izi ndi zotheka kwa yemwe amapanga Wudhu basi. اَلحَمدُ لِلّٰه, Posambitsa nkhope pamene mukupanga Wudhu, nkhopeyo imakhala yotetezeka ku nthenda zochuluka, imathowedwa, kayendedwe ka magazi ku nkhope kamakhala ka mphanvu komanso kabwino, zoyipa zimatha ku nkhope ndipo kawonekedwe kake kabwino kamawonjezereka kawiri.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب　　صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Chitetezo chapa Khungu

Okondedwa abale achisilamu! Pali nthenda imene imachepetsa kapena kutsekula kothelatu kuzungulira komanso kupenya kwa maso zimene zimayambitsa wodwala kukhala wakhungu pang'ono pang'ono. Zotsatira zochuluka za kuchipatala zimasonyeza kuti, ngati zikope za maso zikutsukidwa nthawi

ndi nthawi, matenda owophyawa angathe kupeweka. اَلْحَمْدُ لِلّٰه! Yense wopanga Wudhu ndikusambitsa nkhope yake ndi zachiziwikire kuti zikope za maso ake nazo zimasambitsidwa limodzi. Ndevu za omukonda Mtumiki Wokondedwa (صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم) zimasambitsidwanso pamene akupanga Wudhu zimene zimabweletsa ubwino wochuluka. Dr. yemwenso ndi proffesor George Ail akufotokoza kuti, "Munthu akasambitsa nkhope yake, tizilombo topezeka mu ndevu timachoka. Phata la midzu ya tsitsi limakhala la mphanvu ngati madzi akufikamo. Kupanga Khilal mu ndevu kumachepetsa chiwophyezo cha nsabwe. Kuwonjezera apo, kupezeka kwa chinyezi mu ndevu kumateteza munthu ku matenda okhuza misempha ya khosi, nthenda yogwira chithokomiro komanso kholingo."

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Ubwino wosambitsa zigong'ono

Pali misempha iwiri ikulu ikulu ya magazi imene yadutsa mu zigong'ono imenenso yalumikizana ndi ntima, chiwindi komanso ubongo. Ziwalo za Thupiri limasala chiphimbire. Ngati zigong'ono zanu sizinanyowe komanso sizinaphimbidwe ku m'pweya, matenda ambiri mu ubongo komanso minyewa angayambe. Popanga Wudhu, manja kuphatikizapo zigong'ono zimasambitsidwa ndipo kutero kumalimbitsa ntima, chiwindi komanso ubongo. Mukutero, اِنْ شَآءَاللّٰه, munthu angathe kutetezeka ku matenda okhuza ziwalo zimenezi. Kuwonjezera

apo, ngati manja pamodzi ndi zigong'ono zasambitsidwa, ubale wa munthu umakhazikika ku kuwala kwa chidale chake ndipo kuwalaku kumapangitsa kuyendelera bwino kwa madziwo pa khungu lake. Kusambitsa mapazi nakonso kumalimbitsa misempha yonse ya mudzanja.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب          صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Mawu ubwino wosambitsa ndi kutsuka phazi

Nthawi zambiri Phazi ndi lomwe limakhala ndi fumbi. Mipata ya pakati pa zala za m'miyendo imakhuzika moyambirira. Kusambitsa phazi pamene mukupanga Wudhu kumachotsa fumbi komanso tizilombo toyambitsa matenda. Tizilombo tina totsalira m'menemo timachoka popanga Khilal pakati pa zalazo. Pamene mukupanga Wudhu, kusambitsa mapazi motsatira Sunnah kumachotsa matenda ngati kusakhala ndi tulo, nkhungu yamu ubongo, mantha komanso kukhumudwa.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب          صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Madzi osala popanga  wudhu

Imam Ahmad Raza Khan رحمۃ اللّٰہ علیہ akufotokoza kuti Mtumiki Wokondedwa صلّی اللہ علیہ واٰلہٖ وسلّم anapanga Wudhu ndikumwa madzi osalawo atayima. Zinanenedwa mu Hadith ina yolemekezeka kuti amenewa ndi machiliso a nthenda zokwana

makumi asanu ndi awiri ( 70 ). Zinafotokozedwa mu buku lotchedwa Fatih Al-Moeen, "Ndi Sunnah kumwa madzi osala popanga Wudhu mukamaliza chifukwa kumakhala kuchita monga momwe Hadith yodalitsika yanenera, 'Madzi osalira popanga Wudhu ali ndi machilitso ku nthenda iliyonse.'"

Zokhuza kumwa madzi osala popanga Wudhu, Dotolo wa Chisilamu anati,

1. "Zimathandizira kagwiridwe ntchito bwino ka chikodzodzo, zimachepetsa mavuto amene munthu angakumane nawo potulutsa nkozo.
2. Munthu amatetezeka ku zokhumba zosaloledwa.
3. Zimachotsa kuwotcha kwa chiwindi, m'mimba komanso chikodzodzo."

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب     صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Munthu wofika pa Mwezi

Okondedwa abale a chisilamu! Mutu wa Wudhu komanso sayansi ukumakambidwa. Masiku ano, anthu ochuluka ali ndi chidwi mukufufuza zambiri za sayansi. Anthu otelewa alipo ochuluka m'madela athu amene ali ndi khumbo lalikulu ndi afufuzi a kunja komanso akatswiri a sayansi. Anthu otelewa akuyenera kuzindikira kuti pali nkhani zambiri zomwe

zikufunika kuzindikira zimene akatswiri a sayansi akuyesetsa kupeza mayankho ake, koma Mtumiki Wokondedwa صلى الله عليه وآله وسلم anafotokoza kale zotelezi komanso kuyika mayankho ake. Anthu asayansi tsopano amazinenera mozitamandira kuti amafika ku Mwezi, koma Mtumiki Wokondedwa صلى الله عليه وآله وسلم anayenda ndikupitirira mwezi mu usiku wa Mi'raaj (pomwe ndimalemba bukuli mu mwezi wa Muharram, 1434 pambuyo pa nsamuko wa Mtumiki) zaka 1434 zapitazo. Pamene ndapeza mwayi wokhala pa msonkhano wa chipembezo pa 'Urs ya Imam Ahmad Raza Khan رحمة الله عليه pa Dar-ul-'Uloom Amjadiyyah, 'Nsewu wa Aalamgeer, Bab-ul-Madinah Karachi kumene ndakatulo iyi inatengedwa mu buku lotchedwa Hadaiq Bakhshish:

*Sar Wohi Sar jo Taray Qadamon pay Qurban Gaya*

*Mwana wa Mufti Muhammad Amjad 'Ali A'zami Hanafi* رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه*, mlembi wa ndemanga ya Qur'an yopatulika, 'Allamah 'Abdul Mustafa Azhari* رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه *anapereka ndakatulo yake mu mpikisanowo. Chotsatirachi ndi chigawo cha mavesi awiri kuchokera mu ndakatuloyo:*

*Kehtay hayn Satah pay Chand ki Insan Gaya*
*Arsh-e-A'zam say wara` Tayyaba ka Sultan Gaya*

*Mwachitsanzo, zikunenedwa kuti munthu tsopano wafika ku mwezi. Kunena zowona, mwezi uli pafupi kwambiri; Mneneri wanga wokondedwa* صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم *anapita kutali*

*kwambiri kupyola 'Arsh-e-A'zam (Mpando Wachifumu wolemekezeka wa Mulungu) mu usiku wa Mi'raaj (ulendo wopita kumwamba), n'kusiya mwezi m'mbuyo kutali kwambiri.*

*Arsh ki 'Aql Dang Hay Charkh Mayn Aasmaan Hay*
*Jaan-e-Murad ab Kidhar haye Tira Makan Hay*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

**Chidole cha Kuwala (Nur)**

***Okondedwa abale achisilamu!*** *Mwezi umene asayansi akuti afikapo tsopano, uli pansi pa ulamuliro wa Mtumiki wanga wokondedwa* صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم*. Zikunenedwa m'buku la 'Dalaail-un-Nubuwwah' kuti Sayyiduna 'Abbas Bin 'Abdul Muttalib* رَضِىَ اللّٰهُ عَنْهُمَا*, amalume ake a Mtumiki wokondedwa* صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم*, ananena modzichepetsa kwa Mtumiki wokondedwa* صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم *kuti, "Inu Mtumiki woyera* صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم*! Mu umwana wanu, ndinawona chinthu chomwe chinatsimikizira kuti ndinu Mneneri ndipo ichi ndi chimodzi mwa zifukwa zomwe ndinalandirira Chisilamu. Ndinakuwonani mutagona m'chiri yanu mukulankhula ndi mwezi ndipo mweziwo umayenda kulikonse kumene mumaloza ndi chala chanu chodala." Mtumiki wokondedwa* صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم *anayankha kuti, 'Ndinkalankhula ndi mwezi ndipo nawonso umalankhula ndi ine. Mweziwo umandisangalatsa kuti ndisalire ndipo ndinkamva phokotso la kugwa kwake*


www.dawateislami.net

*pamene umagwa pansi kupanga Sajdah (kugwadira) pansi pa 'Arsh (Mpando Wachifumu) wa Allah Wamphanvu zonse.'*

*Imam Ahmad Raza Khan* رَحْمَةُ اللّٰـهِ عَلَيْه *wanena kuti,*

*Chand Jhuk Jata Jidhar Ungli Uthatay Mahd Mayn*

*Kiya hi Chalta tha Isharon par Khilona Noor Ka*

Munthu wonkonda Mtumiki Wokondedwa wanena kuti,

*Khayltay thay Chand say Bachpan may Aqa Isliye*

*Yeh Sarapa Noor thay wo tha Khilona Noor ka*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Chodzidzitswa chogawa mwezi

Zanendwa mu buku la Sahih Bukhari: Pamene anthu osakhulupirira aku Makkah anamulamula Mtumiki Wokondedwa صَلَّى الله عَلَيهِ وَاٰلِه وَسَلَّم kuti apange chozizitswa chilichonse, iye صَلَّى الله عَلَيهِ وَاٰلِه وَسَلَّم anagawa mwezi mu zidutswa

ziwiri. Mu Vesi 1 ndi 2 ya Surah Al-Qamar, gawo 27, Allah Wamphanvu zonse anati:

اِقْتَرَبَتِ السَّاعَةُ وَانْشَقَّ الْقَمَرُ ﴿١﴾ وَاِنْ يَّرَوْا اٰيَةً يُّعْرِضُوْا وَيَقُوْلُوْا سِحْرٌ مُّسْتَمِرٌّ ﴿٢﴾

*Tsiku la Chiweluzo layandikira , ndipo mwezi wagawanika (ndi kulozera kwa Mtumiki Wokondedwa Muhammad). Ndipo ngati iwo (mwachitsanzo anthu osakhulupirira) awona chizindikiro, amayang'ana nkhope zawo kumbuyo nati, 'Awa ndi matsenga owonekera'*

Kuyikira Ndemanga pa Vesi ili m'mwambayi وَ انْشَقَّ الْقَمَرُ *Kumasulira: ndipo mwezi wagawanika*, Mufti Ahmad Yar Khan رحمۃ اللّٰہِ علیہ akufotokoza, "Mu Vesi imeneyi mwatchulidwa chozizitswa china chachikulu cha Rasool Wokondedwa صلّی اللہ علیہ واٰلہٖ وسلّم 'choziziswa [cha] kugawanitsa mwezi kawiri'.

| | |
|---|---|
| *Isharay say Chand Cheer diya* | *Chupay howe Khoyr ko Phayr liya* |
| *Gaye howe Din ko Asr Kiya* | *Yeh Taab o Tuwan Tumhare Liye* |

صَلُّوْا عَلَی الْحَبِیْب صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

## Chifukwa cha Allah Wamphanvu zonse basi

Okondedwa abale achisilamu! Muzakhala osangalala mukazaphunzira ndikuzindikira ubwino wopanga Wudhu koma ndikuyenera kukudziwitsani kuti sayansi yonse yakhazikika pa kupenekera. Kafukufuku wa Sayansi sanayambe wakhalapo chiganizo kapena kafukufuku womaliza; kumakhala kusintha nthawi ndi nthawi. Komabe, malamuro a Allah Wamphanvu zonse komanso Mtumiki wake Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi omaliza komanso sazasintha mpaka kale. Tikuyenera kumatsatira ma Sunnah ndi cholinga chomusangalatsa Allah Wamphanvu zonse basi, osati kufuna kupeza phindu la zachipatala. Choncho, ngati munthu wapanga Wudhu ndi cholinga chofuna kuchepetsa kathamangidwe ka magazi ake kapena kupeza m'pumulo wabwino, ayenera kusala kudya kuti thupi lake likhale la thanzi komanso kuwoneka bwino, akuyenera kupita ku Madinah kuti asinthe nyengo komanso kusamalira banja lake ndi kuvuta kwa malonda. Komabe, ngati tingamapange ndi cholinga chomusangalatsa Allah Wamphanvu, tizapeza zabwino chifukwa zili ndi ubwino ochuluka. Pa chifukwa ichi, tikuyenera kupanga Wudhu ndi cholinga chofuna kumusangalatsa Allah Wamphanvu zonse kutengera kunja komanso nkati.

## Khalidwe lopambana la Madani la Usufi

Sayyiduna Imam Muhammad Bin Muhammad Bin Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه wanena kuti, "Ukayimika Salah

pambuyo poti wapanga Wudhu, lingalirani chilungamo cha kuti mwayelesa ziwalo za kunja kwa thupi limenenso anthu akutha kuliwona, koma sizolondola kuti munthu apemphere kwa Allah Wamphanvu zonse popanda kuyelesa ntima wanu chifukwa Allah Wamphanvu zonse amayang'ana ntima wanu." Walankhulanso kuti, "Pambuyo poti munthu wapanga Wudhu, akuyenera kukumbukira kuti kuyera kwa ntima kwagona pa kulapa machimo, kusiya uchimo komanso kukhala ndi makhalidwe abwino. Munthu yemwe samayeresa ntima wake ku unve wa uchimo ndikuyika chidwi cha ntima wake kunja kwa thupi komanso kukongola kwake ali ngati yemwe wayitana mfumu ku nyumba yake, kukolopa komanso kuyiwalisa kunja ndi cholinga chofuna kuyisangalatsa mfumuyo ndikusiya nkati mosasamalika. Nanga mfumu ingazayamikire komanso kusangalasidwa ndi munthu woteleyu? Aliyense wa nzeru atha kuzindikira komanso kuganiza m'mene mfumuyi inganvere mu ntima pa munthuyu."

## Sunnah siyikufunikira chitsimikizo cha sayansi

Okondedwa abale achisilamu! Kumbukirani! kuti Sunnah za Mtumiki Wokondedwa صلّى الله عليه واله وسلّم sizikufunika chitsimikizo cha sayansi. Cholinga chathu sikutsatira sayansi, koma Sunnah. Pamene akatswiri a Chizungu anazindikira ndikukhazikitsa pambuyo pofufuza kwa zaka zochuluka kuti, ndi Sunnah za Mtumiki Wokondedwa yekha صلّى الله عليه واله وسلّم.

zimene palibe ngakhale munthu angalemele motani mu umoyo uno, sadzapeza ntendere wa mu ntima. kupatula mu kumukumbikira Allah Wamphanvu zonse yemwe amapereka ntendere wa mu ntima. Chimodzi modzi, munthu angapeze ntendere wa mu ntima pokhala ndi chikondi pa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَالِهٖ وَسَلَّم. Munthu angapeze kukhazikika kwa ntima pa zinthu za dziko la pansi ngati angatsatire ma Sunnah, osati powonera Kanema wa TV, VCR kapena Intaneti. Ngati ukufunisitsadi kukhala ndi kukhazikika kwa ntima mu moyo uno komanso uli nkuza, yimikani Salah tsiku lililonse komanso tsatirani ma Sunnah mokhazikika. Ndipo ngati njira imodzi yofuna kuphunzira bwino ma sunnah komanso mosavuta, yendani pamodzi ndi Madani Qafilah a Dawat-e-Islami pafupi pafupi. Munthu wina aliyense akuyenera kuyika chitsimikizo choyenda ndi Madani Qafilah kwa miyezi khumi ndi iwiri motsatizana kosachepera kamodzi mu umoyo wake wonse, kwa masiku makumi anayi mu miyezi khumi ndi iwiri ndipo masiku atatu pa mwezi wonse.

*Tayri Sunnaton pay Chal kar Mayri Rooh Jab Nikal kar*

*Chalay tum galey lagana Madani Madinay waley*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب          صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ وَالصَّلٰوةُ وَالسَّلَامُ عَلٰى سَيِّدِ الْمُرْسَلِيْنَ اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ

## KUTI MUKHALE MSILAMU WOPEMBEDZA KOMANSO WOPEMPHERA SWALA

Muzikhala usiku wonse mu Ijtima' yapasabata yolimbikitsa Sunnah-Ya Dawat-e-Islami yomwe imachitika Lachinayi lililonse pambuyo pa Swalat-ul-Maghrib munzinda wanu, chifukwa chokondweretsa Allah عَزَّوَجَلَّ ndi zolinga zabwino. Kuti muphunzire ma Sunnah, khalani ndi chizolowezi choyenda ndi Madani Qafilah ya masiku atatu mwezi uliwonse ndi okonda Mtumiki (Rasool), pakulemba nkabukhu konse ka Madani In'amat tsiku lililonse kuchita Fikr-e-Madinah ndikukapereka kwa m'bale wa Chisilamu woyenera wa m'dera lanu pa tsiku loyamba la mwezi uliwonse wa Madani (chisilamu).

**Cholinga Changa Cha Madani:** 'Ndiyenera kuyesetsa kudzikonza ndekha ndi anthu a dziko lonse lapansi, اِنْ شَآءَاللّٰه عَزَّوَجَلَّ.' Kuti tidzikonze tokha, tiyenera kuchita malinga ndi Madani In'amat ndikuyesetsa kukonza anthu a dziko lonse lapansi, tiyenera kuyenda ndi ma Madani Qafilah, اِنْ شَآءَاللّٰه عَزَّوَجَلَّ.

ISBN 978-969-631-813-2

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagaran
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan
UAN: +92 21 111 25 26 92 | Ext: 7213
Web: www.dawateislami.net | E-mail: translation@dawateislami.net